

0B. KUPELEKA MAPHUNZIRO APAMWAMBA OFIKILA MAYIKO OWOPA YEHOVA

B. KUPELEKA MAPHUNZIRO APAMWAMBA OFIKILA MAYIKO OWOPA YEHOVA.

- Ndi ndani oyenela kuti aphunzitsidwe? Aphunzitsi ndi omwe atadzakhale aphunzitsi. Ili ndi phuinziro lachiwiri lomwe likuyenela kuphunzitsidwa ndi mphunzitsi yemwe ali kale ndi lutha la kaphunzitsidwe ndipo mu phunzilori, ophunzitsayu apatsidwa luntha la m'mene angakaphunzitsile poyang'ana zikhaldidwe za mayiko osiyanasiyana.
- Zida zothandizila ophunzitsa – bukhu la malembo oyenela ndi zina mwa zida zomwe amagwilitsa ntchito mu zikhaldidwe zosiyanasiyana

TIYAMBE NDI KUKAMBA ZA CHIKHALIDWE

- Chikhalidwe ndi mmnene kagulu ka anthu kmakhalira kuganizada ndi kukhulupilira. Zikhaldidwe zimapangidwa ndi anthu ndipo muzikhaldidwe mumapezeka zinthu zabwino ndi zoipa zomwe.

KUPHUNZILA ZA CHIKHALIDWE CHA MALO OMWE MULI

- Afunseni okhulupilira a malo omwe muli za nfungo zoipa zomwe ziliponso. Ziganizileni nfungozi bwinobwino ndipo mufananize ndi zomwe inuyo mumaziwona tsiku ndi tsiku.
- Mu bukhu la chipangano chatsopano osankhidwa amumulungu anali ndi zawo zofowoka mu chikhalidwe chawo.
- Mawu a mulungu ndi okhawo omwe ali pamwamba pa zikhaldidwe zones zamayiko osiyanasiyana ndipo chikhalidwe chilichonse chizaweluzidwa chilichonse pachokhapachokha.

Kuweluza chikhalidwe pogwilitsa ntchito mawu a mu bukhu lopatuluka.

- Zimenezi zikhoza kuchitika bwino mu mayiko omwe akuziwa bwino za chikhalidwe chawo komanso omwe ndi okonzeka kuziwa kalikonse kokhudza mulungu.
- Poweluza zikhaldidwe, musagwilitse ntchito njira yoti anthu iwavuta kumva koma awunikileni anthu pa zomwe mawu a mulungu akunena pa zikhaldidwe zanthu.
- Pokonza zikhaldidwe tigwiritse ntchito mawu a mu bukhu loyela komanso tionesese kuti sitikukakamiza anthu kuti apange zomwe tikufuna.

Prepared by Every Child Ministries

"Hope for the forgotten children of Africa"

Translated into Chichewa by Victor K. Phiri

email: ecmafrica@ecmafrica.org

0B. KUPELEKA MAPHUNZIRO APAMWAMBA OFIKILA MAYIKO OWOPA YEHOVA

- Cholinga cha chipunzisochi si kusintha chikhalidwe ayi koma kumuphunzitsa munthu kuti akathe kuwona choipa chomwe chili mu chikhalidwe chake. Kusintha chikhalidwe kumatenga nthawi. Mawu a mulungu ali ngati njele, ngati tingaphunzitse bwino ali ndi mphamvu yosintha chikhalidwe.
- Pophunzitsa ziwani kuti ndibwinonso kuyamikila zabwino zonwe zimapezeka mu chikhalidwe chathu. Chasanzo cha zinthuzi ndi monga nyimbo, magule, zosokasoka komanso kupeleka ulemu kwa atsogoleri athu.

B1. TINGAPHUNZILE BWANJI ZA MIYAMBO YOMWE YINGAKHUZANE NDI NTCHITO YATHU YOPHUNZITSA UTHENGA WA MULUNGU

- Kumbukilani kuti kwa dziko, miyambo yonse ya mzikolo ndi yabwino
- Funsani “mumapanga apanga bwanji zinthu zawo?”
- Zimatanthauza chain munthu wina akamapanga zinthuzi.
- Onesesani ndipo funsani mafunso
- Ayendeleni anthu ku nyumba zawo, mumasukulu, chalitchi ndi m’msika mwayi ukapezeka.
- Muonesetse zinthu ngati nthawi yomwe mukupatsidwa kuti tuyankhule, kayankhidwe ndi kafunsidwe kanu ka mafunso ndi ndi chibale chomwe chilipo pakati pa azimayi ndi azibambo.
- Pa maphunzilo anu, onesesani ndipo phunzitsani momwe mungagonjetsele ziphinjo zomwe zikhoza kulepheletsa zolina zanu.

B2. TINGATENGELE BWANJI MIYAMBO YOMWE YINGAKHUZANE NDI NTCHITO YOPHUNZITSA UTHENGA WA MULUNGU

- Azibambo ndi azimayi kukhala moyang'anana mu nyumba ya mulungu.
- Kavalidwe, maka kwa azimayi
- Zipembezo
- Nthawi
- Kugawana mphatso ndi zina zotelo

Prepared by Every Child Ministries

"Hope for the forgotten children of Africa"

Translated into Chichewa by Victor K. Phiri

email: ecmafrica@ecmafrica.org

OB. KUPELEKA MAPHUNZIRO APAMWAMBA OFIKILA MAYIKO OWOPA
YEHOVA

**B3. TINGAPEWE BWANJI KUSAVANA KOBWELA CHIFUKWA CHA
KUSIYANA CHIYANKHULO**

GWIRITSANI NTCHITO ZOMWE ZILI MU B1

- Mvetselani bwino momwe akulankhulira.
- Onetsetsani ziyankhulo za thupi
- Onetsetsani zizindikilo za kumvetsa ndi kusamvetsa mwa anthu omwe mukulankhula nawo.
- Pepesani ngati simumvana bwino mumalongosoledwe anu.
- Afunseni anthu maganizo awo
- Mukhale munthu odekha.

**B4. TINGAKONZE BWANJI ZIPHUNZITSO ZAPADELA ZOPINDULIRA ANTHU
AKUMUDZI**

- Yambani kukonzeka nthawi ya ziphunzitso yidakali kutali.
- Funsani mafunso a zinthu zomwe simukumvetsa.
- Yankhulani ndi anthu osiyanasiyana kuti tuyale ndi maganizo a anthu ambiri.
- Funsani za mavuto ena omwe angapezeke kupatula a ndalama.
- Onetsetsani kuti mukuyankhula mwa chikoka mu ziphunzitso zones kuti mukope anthu ambili.
- Afunseni ana momwe amakhalila ndi momwe amawayang'anila mu makomo mwawo.
- Khalani omasuka ndipo mukhale okonzeka kusintha maganizo ndi ntchito yomwe munakonzeka kuti tuyigwire nthawi zones.
- Onesesani kuti musapeleke lonjezo lilironse pokhapokha ngati mutazakwanilitse lonjezo lanu.

**B5. TINGAGWIRE BWANJI NTCHITO NDI ANZATHU KUTI TIGWILIRE
NTCHITO LIMODZI POFALITSA UTHENGA**

- Mukhale ndi nthawi yocheza ndi kusangalala ndi anzau.

Prepared by Every Child Ministries

"Hope for the forgotten children of Africa"

Translated into Chichewa by Victor K. Phiri

email: ecmafrica@ecmafrica.org

0B. KUPELEKA MAPHUNZIRO APAMWAMBA OFIKILA MAYIKO OWOPA YEHOVA

- Mukhale ndi nthawi yokambilana. Lolani ndi kumva za mavuto ndi zabwino zomwe anzanu anakumana nazo.

Yankhulani za mitima ya anthu. Lolani anzanu kuti alankhulepo za momwe iwowo amaziwonela pawokha. Pali anthu a mitima yosiyana siyana yina mwa iyo ndi iyi.

- Mkango – Anthu a ntima umenewu amakonda kupanga maganizo ndipo safuna kuti amveko maganizo a anzawo. Anthu amanewa amazinva okha ndipo alibe chisoni ndi anzawo.

“Beaver” – anthu awa ndi anthu omwe ali ndi mtima ofuna kugwila ntchito ndipo amakwanilitsa ntchito tawo akapatsidwa ngakhale kuti anthuwa amagwila ntchito modzipeleka, ntchito yimagwilidwa pang’ono.

“Otter” – Anthu antundu uwu amakonda kusangalala, kucheza ndi anthu ndipo sachedwa kupanga ubwezi ndi anthu. Ngakhale kuti anthuwa ndi abwino chotele amalephela kukhala ndi chidwi pogwila ntchito, amalephela kukonzeka kuti agwile ntchito ndipo sakwanisa kumaliza ntchito akapatsidwa.

“Golden Retriever” – Anthu awa ndi anthu omwe amakhuzidwa kwambiri ndi ubwino wa anzawo. Sakondwa akawona kuti anzawo akuvutika ndipo nthawi zambiri samalimbana ndi kuti ntchito yithe ayi. Anthuwa ali ndi vuto loti samayiwala nsanga mavuto omwe awagwela.

Onetsetsani kuti uthenga wapelekedwa momveka bwino bwino ngati pali kusintha pa ndondomeko yiliyonse yomwe yinakonzeka ya ntchito kapena chiphunzitso.

B5b. TINGAPELEKE BWANJI MAGANIZO ANTHU PA GULU.

- Atsogoleri a magulu ayenela kufunsa magulu awo kuti akambilane mmene membala aliyense wapagulupo angapelekele maganizo ake.

Prepared by Every Child Ministries

“Hope for the forgotten children of Africa”

Translated into Chichewa by Victor K. Phiri

email: ecmafrica@ecmafrica.org

0B. KUPELEKA MAPHUNZIRO APAMWAMBA OFIKILA MAYIKO OWOPA YEHOVA

- Kunena mwa tchutchutchu, maganizo amapelekedwa bwino ngati mafuno kusiyana ndi kufotokoza.
- Ameneakupeleka maganizo akuyenela kukhala okonzeka kupeleka zifukwa za maganizo awo.
- Maganizo onse ayenela kuganizilidwa bwino musanasankhepo maganizo omveka bwino

B5c. TINGAPANGE BWANJI CHISANKHO MWANZELU

- Mukuyenela kukhala ndi nsogoleri wanzeru ndi oziwa ntchito yake.
- Zisankho zikuyenela kupangidwa pa gulu ndipo zikuyenela kufotokozedwa ndi gulu lonse.

B5d. TINGAKONZE BWANJI MAVUTO NDI KUSAMVANA

- Ngati pali kusamvana, atengeleni anthu amene akukhuzidwawo pambali ndipo kambilanani nawo moleza mtima ndi mwa chikondi.
- Musalole kuti nthawi yidusepo musanakambilane.
- Pepesani ngati wina wake walakwiliidwa.

B5f. TINGATHANDIZANE NDI KUTUKULANA BWANJI

- Sankhani munthu mmodzi pa gulu lanu tsiku ndi tsiku kuti mumuthandize.
Komanso kuti mumupemphelere mwapadela.
- Aliyense ayankhulepo chabwino chilichonse cha nzake.
- Limbikisani gulu lanu kuti azilembelana makalata olimbikisana.
- Limbikisani gulu lanu kuti azilimbikisana.

B5g. TINGALIMBIKISANE BWANJI ULENDOWATHU UTATHA

-
-
- Kugawana zithuzi
- Atsogoleri amagulu akuyenela kupitiliza kukumana

Prepared by Every Child Ministries

"Hope for the forgotten children of Africa"

Translated into Chichewa by Victor K. Phiri

email: ecmafrica@ecmafrica.org

OB. KUPELEKA MAPHUNZIRO APAMWAMBA OFIKILA MAYIKO OWOPA YEHOVA

- Pitilizani chibale
- Muzipemphelerana

Prepared by Every Child Ministries
"Hope for the forgotten children of Africa"
Translated into Chichewa by Victor K. Phiri
email: ecmafrica@ecmafrica.org